3. Kodi chimachitika nchiyani tikalekeza msanga kupemphera?

________________________________________

==============================================================

Koma ndi chifukwa chiyani tiyenera kukhala nthaŵi yayitali tili kupempherera zinthu zina zake? Ngati Mulungu ali wokonzeka kuyankha mapemphero athu, nanga ndi chifukwa chiyani amachedwa kuyankha? Ichi ndi chifukwa chakuti Mulungu nthaŵi zina angathe kuyankha mapemphero athu m'njira yotisintha. Nthaŵi zina Mulungu amadziŵa kuti sitiri wokonzeka kuti tilandire mayankho a mapemphero athu.

4. Kodi zimatenga nthaŵi kuti Mulungu atisinthe?

________________

==============================================================

Taganizirani za mayi amene amapempherera mwamuna wake kuti akhale Mkhristu. Ndi zoona ndithu kuti mayi uja anali atatembenuka kale mtima, koma mwina mwake analibe chipatso cha Mzimu m'moyo mwake. Mulungu amaona kuti maiyu akamapempherera mwamuna wake pa nthaŵi yaitali, iye amamkonda Mulungu kwambiri kuposa mmene amadzikondera iye yekha. M'njira imeneyi iye amakhala wokula muuzimu. Iye sadzangofuna kuti mwamuna wake angotembenuka mtima kuti apeze umoyo wosabvuta ayi, koma amafunitsitsa kuti atembenuke mtima kuti apeze ulemerero wa Mulungu.

5. Kodi Mulungu adzampatsa mayankho mayiyu mwamsanga pamene atangoyamba kupemphera kumene?

____________________

==============================================================

Nthaŵi zina Mulungu amachedwa kuyankha mapemphero athu chifukwa iye amafuna kutipatsa zoposera zimene timapempha. Iye amafuna kuti tizipemphera mapemphero aakuluakulu. Tikamapitirizabe kupemphera, mapemphero athu amasintha, nakhala opambana kwambiri molingana ndi chifuniro chake. Kumbukirani za Hana m'Buku Lopatulika. Iye analibe ana. Chinthu ichi chosakhala ndi ana chinamubvuta kwa zaka zambiri.

Chaka chilichonse iye anali kupita ku Hema kumene kunali ku-nyumba ya Mulungu kukapemphera, koma Mulungu anaoneka ngati sanalikumva mapemphero ake. Panthaŵi iyi ana a Israyeli sanali kumutsata bwino Mulungu. Ngakhale atsogoleri awonso anali oipa. Mulungu anafuna kusankhapo mtsogoleri watsopano amene akanatha kuŵatsogolera bwino, choncho anachedwa kuya-nkha pemphero la Hana. Pambuyo pake Hana anasintha pemphero lake. Iye anamuuza Mulungu kuti ngati amupatsa mwana wa mwamuna. Hanayo akanamubwezeranso mwanayo kwa Ambuye. Mu-lungu anamuyankha pemphero lake, ndipo mwana wake Samueli, anakhala mtsogoleri wamkulu wa a Israyeli.

6. Kodi chikanachitika ndi chiyani ngati Hana akanangosiya kupemphera patangopita zaka zochepa chabe?

---

Mapemphero sasintha Mulungu kuti akhale okonzeka kuyankha, koma mapemphero ndiwo amatisintha ife. Iwo amatisintha kuti tipemphere mapemphero amene Mulungu akufuna. Amatisi-ntha kuti tikhale okonzeka kulandira mayankho. Nthaŵi zina izi zimatenga nthaŵi yambiri. Mwina mwake inu mwakhala muli kupempherera china chake kwa nthaŵi yaitali. Musalekeze kupemphera. Kapena Mulungu angayese kugwira ntchito pa inu.

7. Kodi mumafuna kuti Mulungu akusintheni kuti ayankhe mapemphero anu?

---

Palinso chifukwa china chimene chimapangitsa kuti mapemphero athu asayankhidwe mwa msanga m'dierekezi ali nayo mphamvu yoletsa kuti mapemphero athu asayankhidwe <u>mwamsanga</u>. Ngati ife tipitiriza kupemphera iye sangathe kuletsa mapemphero athu kuyankhidwa, koma akhoza kuwachedwetsa.

8. Kodi mumakhala ndi mantha akuti Satana adzatsekereza mapemphero anu mukamapitirizabe kupemphera?

---

Taonani zimene zinamuonekera Danieli. Timawerenga mu Danieli mutu 10 kuti Danieli anayamba kupempherera zinthu zina zimene iye anali kuzifuna. Iye analikupemphera ndi kudya pang'ono chabe kokwanira sabata zitatu, koma mapemphero ake sanayankhidwe konse. Ndipo pomaliza, mngelo anabwera kwa iye.

Danieli 10:12-13:

> Pamenepo anati kwa ine, "Usaope Danieli, pakuti kuyambirana tsiku loyamba lija unaika mtima wako kuzindikira ndi kudzichepetsa pamaso pa Mulungu wako, mawu ako anamveka, ndipo ndadzera mawu ako. Koma kalonga wa ufumu wa Perisiya ananditsekereza njira masiku makumi awiri ndi limodzi, ndipo taonani Mikaeli, wina wa akalonga onveka, anadza kundithandiza; ndipo ndinakhala komweko ndi mafumu a perisiya.

Kalonga wa ku Perisiya sanali munthu kapena mmodzi wa angelo a Mulungu. Koma mmodzi wa ziwanda za m'dierekezi amene anali kufunitsitsa kuti atsekereze m'ngelo wa Mulungu kubwera kuti adzayankhe pemphero la Danieli. Koma Danieli anapitirizabe kupemphera mpaka yankho linabwera.

9. Ngati Danieli akanalekeza kupemphera patangotha sabata imodzi kapena ziŵiri, kodi muganiza kuti pemphero lake likanayankhidwa?

____________________

==========================================================

Nthaŵi zambiri mapemphero athu amatsekerezedwa chifukwa chakuti timalekeza msanga kupemphera. Mulungu amafuna kuti tisamalekeze kupemphera. Nthaŵi zina mapemphero amatisintha Nthaŵi zina ndi chifukwa chakuti imeneyi ndiyo njira yakuti Satana angagonjetsedwere. Pali zinthu zambiri zimene zimapangitsa kuti mapemphero athu asamayankhidwe. Koma ngati tipemphera monga mmene amatiphunzitsira Mulungu, ndiye kuti tikhoza kulandira mayankho.

10. Talembani zinthu zisanu zimene zimalepheretsa mapemphero athu kuyankhidwa?

(1) ____________________________________________

(2) ____________________

(3) ____________________

(4) ____________________

(5) ____________________

==========================================================

**********************************************************

MAYANKHO.

9. Ndalandira yankho lako koma sindikhulupirira pemphero lake kuti likadayankhidwa.
2. Pakusapitiriza kupemphera.
5. Ayi, zidzatenga nthaŵi.
10. Tchimo, kusakhululukira, kupempha zinthu modzikonda, kusakhulupirira, kusapitiriza kupemphera.
8. Ayi.
1. Tchimo, kusakhululukira, kupempha zinthu modzikonda, kusakhulupirira.
4. Inde, nthaŵi zina zimatero.
7. Yankhani mmene mungafunire.
3. Mapemphero athu sayankhidwa.
6. Pemphero lake silikanayankhidwa.

SABATA LACHISANU NDI CHIŴIRI: KUKULA M'CHIKHULUPIRIRO
TSIKU LOYAMBA:

Sabata yatha tinaphunzira kuti chimodzi cha zinthu zimene zimatsekereza mapemphero athu ndi kusakhulupirira. Tinawerenga ndime zambiri kuchokera m'Buku Lopatulika zimene zimatilangiza momwe tiyenera kukhalira ndi chikhulupiriro tikamapemphera.

1. Kodi mungakumbukire zinthu zina zimene zimatsekereza mapemphero athu? Tazilembeni apa:

   (1) ________________ (3) ________________

   (2) ________________ (4) ________________

================================================================

Tawerenganinso ndime izi ndipo muone mmene chikhulupiriro chili chofunikira m'mapemphero anu.

Ahebri 11:6:

> Koma wopanda chikhulupiriro sikutheka kumkondweretsa; pakuti iye wakudza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti alipo, ndi kuti ali wobwezera mphotho iwo akumfuna Iye.

Mateyu 17:19-20:

> Pamenepo ophunzira anadza kwa Yesu, ali payekha, nati, Nanga ife sitinakhoza bwanji kuchitulutsa? Ndipo Iye ananena kwa iwo, chifukwa chikhupiriro chanu nchaching'ono: pakuti indetu ndinena kwa inu, mukakhala nacho chikhulupiriro monga kambewu kampiru, mudzati ndi phiri ili, senderapo umuke kuja; ndipo lidzasendera; ndipo palibe kanthu kadzakulakani kosachitika.

Yakobo 1:6-7:

> Koma apemphe ndi chikhulupiriro, wosakayika konse; pakuti wokayikayo afanana ndi pfunde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuŵinduka nayo.

2. Kodi ndi mayankho angati amene tingapeze ngati sitikhala ndi chikhulupiriro m'mapemphero athu? ____________________

==========================================================

Ndipo tikawerenga ndime zimenezi timaona kufunika kwake kwa kukhulupirira Mulungu pamene tipemphera. Tingaonenso kuti Mulungu amafuna kuchita zinthu zodabwitsa kupyolera m'mapemphero athu. Koma choyamba tiyenera kukhulupirira, ndipo pambuyo pake Iye adzachita zimenezi. Ife timafuna kuti Mulungu achite zinthu zimenezi koma chikhulupiriro chathu ndi chochepa. Kodi chikhulupiriro chathu chochepachi tingachikuze bwanji? Izi ndi zimene tikufuna kuphunzira sabata ino.

3. Kodi muli kufuna chikhulupiriro chanu kuti chikule?

____________________

==========================================================

Njira imene timaidziŵa ya mapemphero imene amafuna Mulungu ndiyo yopyolera m'Buku Lopatulika basi. Ife timakhulupirira kuti Buku Lopatulika ndiwo Mawu a Mulungu. M'Buku Lopatulika, Mulungu amatipatsa mawu olimbikitsa chikhulupiriro chathu. Taonani mawu amene Yesu anauza ophunzira ake usiku asanapachikidwe. Timapeza mawuŵa mu Yohane 14, 15 ndi 16. Aŵa ndi mawu ofunika kwambiri. Yesu anali kuŵasiya ophunzira ake kuti iwo azipitirizabe ntchito yake. Iye anadziŵa kuti iwo Iye anadziŵa kuti iwo sadzakhala nayo mphamvu yopitiriza ntchito mwa iwo okha, koma adzafuna chithandizo. Yesu anaŵauza kambirimbiri kuti adzawathandiza ngati iwo adzapemphera.

Yohane 14:13-14:

> Ndipo chimene chilichonse mungafunse m'dzina langa, ndidzachichita, kuti Atate akalemekezedwe mwa Mwana. Ngati mudzapempha kanthu m'dzina langa, ndidzachita.

Yohane 15:7:

> Ngati mukhala mwa Ine, ndi mawu anga akhala mwa inu, pemphani chilichonse chimene muchifukwa ndipo chidzachitika kwa inu.

Yohane 15:16:

Inu simunandisankhe Ine; koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala chipatso, ndi kuti chipatso chanu chikhale; kuti chimene chilichonse mukapempha Atate m'dzina langa akakupatseni inu.

Yohane 16:23-24:

Ndipo tsiku limenelo simudzandifunsa kanthu. Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Ngati mudzapempha Atate kanthu, adzakupatsani inu m'dzina langa. Kufikira tsopano simunapempha kanthu m'dzina langa; pemphani, ndipo mudzalandira, kuti chimwemwe chanu chikwanire.

4. Kodi Yesu anaŵauza kangati ophunzira ake m'ndime izi kuti angathe kupeza mayankho ku mapemphero awo?

________

============================================================

Ngati tifuna kuuza anthu ena chinthu china chofunika timachibwerezabwereza kuti titsimikize kuti zamvekadi.

5. Kodi chinali chofunika kwa Yesu kuti ophunzira ake ayenera kupemphera ndi kupeza mayankho a mapemphero awo?

________________

============================================================

Tikamawerenga mmene Yesu anaŵauzira ophunzira ake kuti mapemphero awo adzayankhidwa, timadziŵa kuti malonjezo aŵa ndi athunso. Timadziŵa kuti Yesu amafunabe kutikumbutsa nthaŵi zambiri kuti tizitha kupeza chithandizo kupyolera m'mapemphero. Ndipo timadziŵa kuti Mulungu amafunitsitsa kuyankha mapemphero athu.

6. Kodi zinathandiza kukuza chikhulupiriro chanu pamene mukukumbukira mmene Mulungu amafunira kuyankha mapemphero anu?

________________

============================================================

Muli malonjezo ena m'Buku Lopatulika amene angathe kulimbikitsa chikhulupiriro chathu. Lonjezo limodzi limene timaliganizira ndi limene limapezeka pa Mateyu 7:7:

> "Pemphani ndipo chidzapatsidwa kwa inu; funani ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo chidzatsekulidwa kwa inu."

7. Kodi chimachitika ndi chiyani ngati ife tibwera kwa Mulungu ndi kupempha?

_______________________________

==================================================

Mateyu 7:7 ndiyo ndime imene ife tingathe kumaibwereza kaŵirikaŵiri pamene tikupemphera ndi kupeza mphamvu za chikhulupiriro chathu.

8. Mukhale muli kuinena kaŵirikaŵiri ndime iyi mpaka mutailoŵeza pamtima. Ndidzakufunsani kuti mudzainene mkalasi.

==================================================

Pano palinso ndime ina imene ingathandize chikhulupiriro chanu.

1 Yohane 3:22:

> Ndipo chilichonse chimene tipempha, tilandira kwa Iye, chifukwa tisunga malamulo ake, ndipo tichita zomkondweretsa pamaso pake.

9. Ngati tikumvera Mulungu, kodi tikhoza kuyembekeza kuti Iye ayankhe mapemphero athu?

_______________________________

==================================================

1 Yohane 5:14-15:

> Ndipo uku ndi kulimbika mtima kumene tili nako kwa kwa Iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa chifuniro chake, atimvera; ndipo ngati tidziŵa kuti atimvera chilichonse tichipempha, tidziŵa kuti tiri nazo izi tazipempha kwa Iye.

10. Pamene tidziŵa kuti tili kupempha chinthu china chimene chili chifuniro cha Mulungu, kodi tingayembekezere chiyani?

_______________________________________________

==========================================================

M'Buku Lopatulika muli ndime zambiri zimene zimalonjeza kuti Mulungu amamva ndipo amayankha mapemphero athu. Sitingathe kuzilemba zonse m'buku lino. Mukamawerenga Buku Lopatulika mudzazipeza. Mukazipeza, mulembe mizere pamunsi pake ndipo muziloweze kuti muzikhala oziganizira mukamapemphera.

11. Kodi mungatani kuti chikhulupiriro chanu chikule?

_______________________________________________

==========================================================

************************************************************

MAYANKHO.

8. Khalani okonzeka kunena pamtima Mateyu 7:7 mkalasi
5. Inde, kunali kofunika.
7. Tidzalandira.
2. Palibe.
6. Yankhani monga momwe muganizira.
10. Tikhoza kuyembekeza kuti adzatimva ndipo adzatiyankha.
1. Tchimo, kusakhululukira, kupempha zinthu modzikonda, kusapitiriza mapemphero.
11. Funani malonjezo a Mulungu m'Buku Lopatulika ndipo muziloweze pamtima.
9. Inde.
4. Kasanu ndi kamodzi.
3. Yankhani monga momwe mukuganizira.

SABATA LACHISANU NDI CHIŴIRI: KUKULA M'CHIKHULUPIRIRO
TSIKU LACHIŴIRI:

Dzulo tinaphunzira chinthu choyamba chimene tingathe kuchita pakulimbikitsa chikhulupiriro chathu.

1. Kodi ndi chiyani? ______________________________

=================================================================

M'Buku Lopatulika timawerenga malonjezo ambiri onena kuti Mulungu adzayankha mapemphero athu. Koma simalonjezo okha amene tili nawo. Tilinso ndi zinthu zimene zinachitika zosonyeza kuti Mulungu amasunga malonjezo ake. Timawerenga nthano za zomwe Mulungu anayankhira pemphero la anthu m'Buku Lopatulika.

2. Kodi zimakuthandizani kukhulupirira munthu wina amene mumamudziŵa kuti anasunga lonjezo kwa anthu ena?

   ____________________

=================================================================

Tikamawerenga Buku Lopatulika, timawerenga za nthaŵi zimene Mulungu anayankhira mapemphero. Timaona kuti Mulungu amasunga lonjezo lake. Tikamaona mmene Mulungu amayankhira mapemphero a anthu ena, chikhulupiriro chathu chimakula chifukwa timakhulupirira kuti Iye adzayankha mapemphero athu.

3. Kodi mungawerenge zotani m'Buku Lopatulika kupatulako za malonjezo wothandiza chikhulupiriro chanu kuti chikule ndi mphamvu?

   ______________________________

=================================================================

Tiyeni tione nthano ya Eliya. Mulungu anayankha mapemphero a Eliya. Choyamba Mulungu anadzetsa njala kuti anthu amukumbukire. Pambuyo pake Mulungu anabutsa moto pa phiri la Karimeli kuonetsa kuti anayankha pemphero la Eliya. Uku kunali kudzisonyeza kuti Iye anali Mulungu woonadi. Pamene

Eliya anapempheranso, Mulungu anapereka mvula pamene kumaloko kunali kopanda mvula kokwanira zaka zitatu. Timawerenga izi pa 1 Mafumu 18. Tatsekulani Buku Lopatulika pa mutu umenewu ndipo werengani ndime 36, mpaka 45 kuti muone mmene Mulungu anayankhira mapemphero a Eliya.

4. Mukatha kuwerenga mbiri iyi, kodi mukukhulupirira kuti Mulungu amayankha mapemphero?

____________________________

==========================================================

Koma tikamaŵerenga mbiriyi timanena kuti, "Inde, Mulungu anayankhadi mapemphero a Eliya, koma Eliya anali ndithu munthu wolemekezeka. Ichi ndi chifukwa chake Mulungu anayankha mapemphero ake." Izi sizimene Buku Lopatulika limanena ayi. M'Chipangano Chatsopano Yakobo amatiuza kuti Eliya anali munthu ngati ife, komabe Mulungu anamuyankha mapemphero ake.

Yakobo 5:17-18:

> Eliya anali munthu wakumva zomwezi tizimva ife, ndipo anapemphera chipempherere kuti isabvumbwe mvula ndipo siinagwa mvula pa dziko zaka zitatu kudza miyezi isanu ndi umodzi. Ndipo anapempheranso; ndipo m'mwamba munatsika mvula, ndi dziko lidabala zipatso zake.

5. Kodi Mulungu anayankha mapemphero a Eliya chifukwa chakuti iye anali munthu wolemekezeka?

_________________

==========================================================

Zimatithandiza tikamakhulupirira kuti Mulungu akhoza kuyankha mapemphero athu tikawerenga mmene Iye anayankhira mapemphero a Eliya. Tikhoza kukulitsa chikhulupiriro chathu tikawerenga momwe Mulungu anayankhira mapemphero a Yesu. Yesu anali kupemphera kwa Mulungu kaŵirikaŵiri. Ndipo Mulungu anali kuyankha mapemphero ake. Tingoona kamodzi kokha za zimenezi. Pa Yohane mutu 11, Yesu anali chiimirire pamphepete pa manda a bwenzi lake, Lazaro. Tsekulani Buku Lopatulika pa Yohane 11 ndipo werengani ndime 39 mpaka 44 muone chimene chinachitika.

6. Kodi Yesu anachita chiyani asanamulamule Lazaro kuti auke?

_______________

==================================================

Yesu anadziŵa kuti Mulungu anamva mapemphero ake. Iye anati "Ndimadziŵa kuti mumandimva nthaŵi zonse." Nanga chikhulupiriro chathu chimathandizidwa bwanji ndi zimenezi? Yesu anali Mwana yekhayo wobadwa yekha wa Mulungu. Ndithudi Mulungu anamumvera ndipo anamuthandiza kuchita zodabwitsa. Koma taonani zimene Yesu anauza ophunzira ake.

Yohane 14:12:

"Indetu ndinena kwa inu, Wokhulupirira Ine, ntchito zimene ndichita Ine, adzazichitanso iyeyu, ndipo adzachita zoposa izi, chifukwa ndipitita Ine kwa Atate!"

7. Kodi Yesu amanena kuti ophunzira ake adzachita ntchito zotani?

_______________

==================================================

Tiyeni tionenso nthaŵi ina imene Mulungu anayankhira mapemphero a anthu ena m'Buku Lopatulika. Pa Machitidwe mutu 4 ophunzira ena adaikidwa m'ndende chifukwa chakuti anali kulalikira za Yesu. Patangopita kanthaŵi olamulira anaŵamasula, koma anaŵauza kuti asalalikirenso za Yesu. Kodi ophunzira aja anachita chiyani? Anapemphera kuti Mulungu aŵalimbikitse kupitirizabe kulalikira za Yesu Khristu. Tsekulani Buku Lopatulika ku Machitidwe 4 ndipo muwerenge ndime 23 mpaka 31.

8. Kodi Mulungu anayankha bwanji mapemphero a anthu ameneŵa?

_______________

_______________

==================================================

9. Kodi kumatithandiza mwa njira yanji tikamawerenga nthano za mapemphero amene anali kuyankhidwa ndi Mulungu m'Buku Lopatulika?

__________________________________________

______________________________________________________

10. Kuchokera mphunziro ili, kodi tiyenera kuchita chiyani pa kulimbikitsa chikhulupiriro chathu?

______________________________________________________

______________________________________________________

============================================================

************************************************************

MAYANKHO.

1. Kuwerenga Buku Lopatulika.
3. Nthano za momwe Mulungu anayankhira mapemphero a anthu ena.
5. Ayi.
7. Zinthu zikuluzikulu.
9. Kumatipatsa chikhulupiriro.
2. Inde.
4. Inde.
6. Anapemphera.
8. Anaŵalimbikitsa
10. Ŵerengani mmene Mulungu adayankhira pemphero m'Buku Lopatulika.

SABATA LACHISANU NDI CHIŴIRI: KUKULA M'CHIKHULUPIRIRO
TSIKU LACHITATU:

Taphunzira kuti pali zinthu ziŵiri m'Buku Lopatulika zimene tingathe kuwerenga kuti tilimbikitse chikhulupiriro chathu.

1. Kodi ndi zinthu ziŵiri zotani?

   (1) ____________________________________________

   (2) ____________________________________________

==========================================================

Chinthu china chimene timachidziŵa kuti chimalimbikitsa chikhulupiriro chathu ndicho kutaya zinthu zimene timazidziŵa kuti ndizo zimatsekereza mapemphero athu.

2. Kodi ndi chiyani chimene chili m'mitima yathu chimene chimalepheretsa mapemphero athu kuyankhidwa?

   ____________________________________________

==========================================================

Ngati tikufuna kuti tikhulupirire malonjezo a Mulungu, tiyenera kudziŵa ngati tilibe tchimo limene lingamuletse Mulungu kuyankha mapemphero athu. Koma, tingathe kudziŵa bwanji? Nanga tingatsimikize bwanji kuti mitima yathu ili yoyera? Tikhoza kumpempha Mulungu kuti atisonyeze ngati pali tchimo lililonse limene sitinalibvomereze, ndipo Iye adzatisonyeza.

Yeremiya 17:9-10:

> Mtima ndiwo wonyenga koposa, ndi wosachiritsika, ndani angathe kuudziŵa? Ine Yehova, ndisanthula mtima, ndiyesa imso, kuti ndimpatse munthu yense monga mwa njira zake, monga zipatso za ntchito zake.

3. Ngati Mulungu amalonjeza kuyankha mapemphero athu, kodi Iye adzatisonyeza tchimo limene lili m'mitima mwathu tikampempha kuti atisonyeze?

Kodi tidzachita chiyani ngati tipeza tchimo m'mitima mwathu pamene tili kupemphera? Timadziŵa kuti Mulungu sadzamvera mapemphero athu pamene mumtima mwathu muli machimo. Tiyenera kuchotsa tchimo limeneli.

4. Kodi tchimo tingalichotse bwanji m'mitima mwathu?

____________________________________________________

============================================================

Mulungu amalonjeza kutikhululukira machimo athu ngati titaŵabvomereza.

1 Yohane 1:9:
Ngati tibvomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse.

Nthaŵi zina timaŵachimwira anthu ena. Timapempha Mulungu kuti atikhululukire, koma tiyenera kuyanjana ndi anthu ena. Kumbukirani zimene zinanenedwa ndi Zakeyu pamene anatembenuka mtima.

Luka 19:8:
Ndipo Zakeyu anaimirira nati kwa Ambuye, "Taonani Ambuye, gawo limodzi la zanga zonse zogaŵika pakati ndipatsa osauka; ndipo ngati ndalanda kanthu kwa munthu monyenga, ndim'bwezera kanayi."

5. Nanga ukamubera munthu wina zinthu zake, ndipo mupanda kumubwezera zinthuzo, kodi Mulungu adzamvera pemphero lako?

________________

============================================================

Pamene ife timabvomereza machimo athu kwa Mulungu, ndipo pamene tiyanjana ndi anthu ena, timadziŵa kuti mitima yathu ndiyoyera kotero kuti tikhoza kukhulupirira kuti Mulungu alikumva mapemphero athu.

1 Yohane 3:21-22:
Okondedwa, mtima wathu ukapanda kutitsutsa, tili nako kulimbika mtima mwa Mulungu; ndipo chimene chilichonse tipempha, tilandira kwa Iye, chifukwa tisunga malamulo ake, ndipo tichita zomkondweretsa pamaso pake.

6. Ngati mitima yathu imatidzudzula, kodi tingathe kukhala ndi chikhulupiriro kwa Mulungu?

____________________

7. Ngati titafufuza m'mitima mwathu ndipo Mulungu akutisonyeza kuti ili yoyera, kodi chimachitika ndi chiyani ku chikhulupiriro chathu?

______________________________

============================================================

************************************************************

MAYANKHO.

7. Chimakula ndi mphamvu.
5. Ayi.
3. Inde.
1. (1) Malonjezo a Mulungu. (2) Mbiri za mmene Mulungu anayankhira mapemphero a anthu ena.
6. Ayi.
4. Kutembenuka mtima ndi kupempha Mulungu kuti atikhululukire.
2. Tchimo.

SABATA LACHISANU NDI CHIŴIRI: KUKULA M'CHIKHULUPIRIRO
TSIKU LACHINAYI:

Kuchokera kumaphunziro a masiku atatu apitaŵa, kodi mwaphunzira chiyani za mmene tingalimbikitsire chikhulupiriro?

1. Lembani mizere pang'ono zimene mwaphunzira.

______________________________________________

______________________________________________

==================================================

Nthaŵi zambiri m'Buku Lopatulika pamene Yesu anali kuchiritsa anthu Iye anali kunena kuti iwo amachira chifukwa cha chikhulupiriro chawo.

Mateyu 9:22:
Koma Yesu potembenuka ndikuona iye anati, "Limba mtima, mwana wamkaziwe, chikhulupiriro chako chakuchiritsa." Ndipo mkaziyo anachira kuyambira nthaŵi yomweyo.

Mateyu 9:28.29:
Ndipo mmene iye analowa mnyumba, akhunguwo anadza kwa Iye, ndipo Yesu anati kwa iwo, "Mukhulupirira kodi kuti ndikhoza kuchita ichi?" Anena kwa Iye "Inde, Ambuye." Pomwepo anakhudza maso awo; nati, "Chichitidwe kwainu monga chikhulupiriro chanu."

Mateyu 15:28:
Pomwepo Yesu anayankha, nati kwa iye, "Mkaziwe, chikhulupiriro chako ndi chachikulu! Chikhale kwa iwe monga momwe wafunira!" Ndipo mwana wake anachira nthaŵi yomweyo.

2. Kodi anthu aŵa anakhulupirira Mulungu? ________

==================================================

Koma anthu sanali kungom'khulupirira Yesu mwamsanga ndi mosabvuta ayi. Ngakhale ophunzira ake amene nthaŵi zina sanali kukhulupirira. Nthaŵi zambiri Yesu anali kuŵauza kuti chikhulupiriro chawo chinali chaching'ono.

Mateyu 8:26:

Ndipo ananena Iye kwa iwo, "Muli amantha bwanji? Okhulupirira pang'ono inu!" Pomwepo Iye anauka nadzudzula mphepo ndi nyanja, ndipo panagwa bata lalikulu.

3. Kodi ophunzira aja anali ndi chikhulupiriro chachikulu pa nthaŵi imeneyi?

______________________

Kodi Yesu anaŵathandiza ngakhale chikhulupiriro chao chinali chochepa?

__________________________________

==============================================================

Nthaŵi zambiri timakhala ngati ophunzira a Yesu aja. Iwo anadziŵa kuti chikhulupiriro chawo chinali chaching'ono, ndipo anapempha Yesu kuti aŵathandize.

Luka 17:5-6:

Ndipo atumwi anati kwa Ambuye, "Mutionjezere chikhulupiriro." Koma Ambuye anati, "Mukakhala nacho chikhulupiriro ngati kambewu ka mpiru, mukanena kwa mtengo uwu wamkuyu, "Uzulidwe, nuokedwe m'nyanja, ndipo akadamvera inu."

4. Kodi atumwi anapempha ndani kuti aŵathandize m'chikhulupiriro chawo?

______________________________________________________

==============================================================

Pano pali chinthu china chimene tikhoza kuchita kuti tikuze chikhulupiriro chathu. Tikhoza kumpempha Mulungu kuti ationjezere. Yesu sanadzudzule ophunzira ake pamene anapempha chikhulupiriro. Iye anathandiza chikhulupiriro chawo poŵauza kuti ngakhale chikhulupiriro chaching'ono chikhoza kupanga zinthu zazikulu.

5. Ngati muli ndi chikhulupiriro ngakhale chaching'ono, kodi Mulungu adzamvera mapemphero anu?

________________

==========================================================

M'Buku Lopatulika munali munthu wina amene anali ndi mabvuto ndi chikhulupiriro chake. Munthu ameneyu anali ndi mwana wa ziŵanda, kapena kuti mzimu woipa. Iye anadza ndi mwanayo kwa Yesu ndipo anampempha kuti atulutse chiŵandacho mwa mwanayo.

Marko 9:23-24:

> "Ndipo Yesu ananena naye, Ngati mukhoza! Zinthu zonse zitheka ndi iye wakukhulupirira. Pomwepo atate wa mwana anapfuula, nanena, Ndikhulupirira; thandizani kusakhulupirira kwanga."

6. Kodi bambo uja anatani pamene anaona kuti chikhulupiriro chake chinali chaching'ono?

________________________________

________________________________

==========================================================

7. Kodi tingachite chiyani pamene chikhulupiriro chathu chili chaching'ono?

________________________________

________________________________